WEEKEND NATION
LOWERUKA, 17 DECEMBER, 2022




CHITHUNZI: MARTIN GELA JNR

Ntchito yokumba ngalande kuchigwa cha Shire ili mkati

# Amayi nawo azipindula ndi malo paulimi

**WOLEMBA: MARTIN GELA JNR**

Anthu okhala m'dera la gulupu Fombe, T/A Kasisi m'boma la Chikwawa ati ndi wokondwa ndi ntchito ya kalembera wa malo yomwe ikuchitika m'bomali pansi pa pulojekiti ya Shire Valley Transformation Programme (SVTP).

Poyankhulapo atayenderedwa ndi wachiwiri kwa nduna ya za malo a Deus Gumba omwe anadzaona ntchitoyi, mmodzi wa mamembala akomiti yoyang'anila za malo kwa Fombe a Charles Chilenje anati ntchito yakalembera wa maloyo ikuyenda bwino ndipo ambiri amene alembetsa malo awo ndi amai.

A Chilenje anati: "Ndine wokondwa kuti amayi ambiri akulembetsa malo kukhala m'maina awo. Izi zikulimbikitsa umwini wa malo. Kuno kwathu poyamba timakhulupilira kuti mayi sakhala ndi malo. Akachoka kwawo kupita kubanja amataya umwini wa china chilichonse kuphatikizapo malo, komanso banja likatha kapena mwamuna akamwalira amabwelrra kwawo chimanjamanja."

Iwo adati kalembela wa maloyu akuthandizira kuti amai ndi ana asamavutike zovuta zikawaonekera.

"Izi zimapangitsa kuti tizikhala ndi njala popeza kunena mosabisa mwini ulimi ndi mayi abambo nthawi zambiri amathawathawa," anatero a Chilenje.

Boma linaonetsetsa kuti anthu onse amene adzapindule ndi pulojekiti ya SVTP alembetsa malo awo kuti akhale ndi umwini. Anthuwa adzalandira ziphaso zotsindika umwini wa malo awo zomwe zidzathandize kuti asonkhanitse pamodzi malo awo kuti azichita ulimi wamthirira wa makono. Alimiwanso azidzatha kugawana phindu kutengera ndi kukula kwa malo awa. Izi zidzapititsa patsogolo ntchito za ulimi.

A Gumba adati ndi wokondwa kuti amayi nawo ayamba

kukhala ndi umwini wa malo.

Iwo adati: "Malamulo okhudza za malo omwe mtsogoleri wa dziko lino a Lazarus Chakwera anasayinira akupereka umwini kwa nzika za dziko lino kuti zizikhala ndi umwini wa malo. Munthu akapatsidwa satifiketi ya umwini wa malo ndipo akapezeka kuti wamwalira, satifiketiyi imakhala ndi mkazi wake ndipo iyenso akamwalira chitupa cha malo chimakhala ndi ana omwe amayenera kupindula ndi malowo."

Mneneri wa SVTP, Alice Kaunda anati kupyolera m'kalembera wa maloyu, malo okwanira 46 149 omwe ndi mahekitala 23 392 analembedwa m'gawo loyamba la pulojekitiyi. Iwo anati izi zidzapititsa patsogolo ntchito za ulimi wa makono molingana ndi masomphenya a boma pachitukuko ya Malawi 2063 yomwe ikulimbikitsa kupanga ulimi ngati bizinezi.

A Kaunda akulimbikitsa anthu m'chigwa cha mtsinje wa Shire komanso madela ena kuti akalembetse mkaundula wa za malo adindo akafika m'dera lawo poti izi zidzalimbikitsa umwini wa malo kwa mibado ili nkudza. ■




Ntchito zaulimi kunjaku ndiye zagundika. Alimi ayenera kudziwa mitengo ya zina ndi zina zofunika. Mitengoyi idali chonchi pa 4 October 2022:

**Matumba osungira chimanga**

| | |
|---|---|
| A makilogalamu 50 | Ayambira K200 |
| A makilogalamu 90 | Ayambira K400 |
| Amakilogalamu 100 | Ayambira K450 |
| A makilogalamu 200 | Ayambira K600 |

**Matumba a Pics Bags**

| | |
|---|---|
| A makilogalamu 50 | Ayambira K1 700 |
| A makilogalamu 100 | Ayambira K2 300 |

**Zoyanikira chimanga**

| | |
|---|---|
| Za matumba | Zayambira K4 000 |
| Malona | Zayambira K7 500 |

**Zosolera chimanga**

| | |
|---|---|
| Makina osolera chimanga a dizilo | Ayambira K900 000 |
| Makina osolera chimanga a magetsi | Ayambira K600 000 |

**Mankhwala ophera anankafumbwe**

| | |
|---|---|
| Falcon (magalamu 150) | |
| Super Shumba (magalamu 200) | Ayambira K1 700 |
| Atelic Super Dust (magalamu 250) | Ayambira K1 950 |
| Super guard (magalamu 200) | Ayambira K4 00 |
| Novatellic (magalamu 200) | Ayambira K4 000 |
| Weevil kill (magalamu 200) | Ayambira K1 700 |
| Ghanrai (mamililita 200) | Ayambira K2 000 |
| Ghanrai (mamilita 500) | Ayambira K3 000 |
| Ghanrai (lita imodzi) | Ayambira K6 000 |
| Cropchem (Lita imodzi) | Wayambira K9 500 |

**Mankhwala ophera makoswe**

| | |
|---|---|
| Ratcide (magilamu 100) | Wayambira K2 000 |
| Latex (magilamu 100) | Wayambira K1 000 |
| Rat Guard (magilamu 100) | Wayambira K1 000 |

**Mankhwala opha tizilombo ku tomato**

| | |
|---|---|
| Cypermethyline (mamililita 100) | Wayambira K1 500 |
| Dithane (magilamu 200) | Wayambira K2 000 |
| Copper (magilamu 200) | Wayambira K2 000 |
| Ventum (mamililita 250) | Wayambira K1 500 |

**Zipangizo zopopera mankhwala ku mbewu**

| | |
|---|---|
| Za malita 16 | Zayambira K8 000 |
| Za malita 20 | Zayambira K10 000 |

**Mankhwala a nkhuku**

| | |
|---|---|
| Lasota womwetsa nkhuku 100 | Wayambira K1 500 |
| Hitchner womwetsa nkhuku 100 | Wayambira K1 500 |

**Mankhwala opha njoka za m'mimba ku ziweto**

| | |
|---|---|
| Piperazine (magilamu 30) | Wayambira K2 000 |
| Abendazo (magilamu 100) | Wayambira K3 000 |

*Tiuzeni umo mitengo ikuyendera kwanuko potumiza uthenga pa 0888412807*